UMBONI WANGA

Enoch Kamanula

New Testament Assembly
P.O. Box 64,
Mwanza, Malawi.

"Ndipo Mau ndinawamva ochokera Kumwamba, analankhulanso nane, nanena, Muka, tenga bukhu lofunyululalo m'dzanja la mngelo wakuimirira panyanja ndi pa dziko. Ndipo ndinamuka kwa mngelo, ndi kunena naye, Ndipatse kabukhuko. Ndipo ananena ndi ine, Dzatenge, nudye; ndipo kadzawawitsa m'mimba mwako, komatu m'kamwa mwako kadzazuna ngati uchi. Ndipo ndinatenga kabukhu m'dzanja la mngelo, ndipo ndinakadya; ndipo kanali mkamwa mwanga kozuna ngati uchi; ndipo pamene ndinakadya m'mimba mwanga mudawawa. Ndipo ananena nane, Uyenera iwe kuneneranso pa anthu ndi mitundu, ndi manenedwe, ndi mafumu ambiri."

{Chivumbulutso 10:8-11}

UMBONI WANGA

Enoch Kamanula

Ine ndinabadwira ku Malawi mu banja la Emmanuel ndi Mary Kamanula pa 31 December, 1974 mu njira ya opareshoni. Ndiri wa zaka ziwiri Mulungu anandichiritsa ine ku mabala woopsa pamene poto wa madzi otentha anandikhuthukira. Ine ndinali pafupifupi kufa ndipo makolo anga analibe chiyembekezo kuti ndikanatha kukhala ndi moyo. Bambo wanga amagwira ntchito ngati mlangizi, nthawi imeneyo ku Chikwawa kumwera kwa Malawi. Dera limeneli limatchulidwanso kuti Shire Valley ndipo ndi amodzi mwa malo otentha kwambiri ku Malawi. Ine ndinachiritsidwa ndipo ichi chinali chozizwa ku banja lathu. Kuchiritsidwa kwanga kunalimbikitsa banja lathu chifukwa wina amatengedwa ngati osasamala. Kenako makolo anga anasamuka kupita kukagwira ntchito ku katauni kena kakang'ono kotchedwa Nsanje komweko ku Shire Valley ndipo kumeneko ndi kumene ndinakachita maphunziro anga a Pulaimare. Pamene ndinali nyamata wang'ono ndimakonda kuwedza nsomba ndipo ndimapita ndi amzanga kukawedza mu Mtsinje wa Shire.

Mu 1982, ife tinamva za M'bale William Branham, Mneneri wam'thenga wa Mulungu kukwaniritsa Malaki 4:5 komanso Chivumbulutso 10:7. Bambo wanga anakhulupirira Uthenga wa M'bale Branham ndipo anabatizidwa chaka chomwecho. Kagulu kakang'ono kanayambika ku Nsanje ndipo M'bale Palinji Bobo anali M'busa. Ngati chisamba m'banjamo, ine ndimakhudzidwa kwambiri ndi kunyamula mipando kupita nayo pa mtengo wa Mango pamene timasonkhaniranapo. Ine ndinabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu mu 1985 ndiri ndi zaka 10.

Ine ndikukumbukira bambo wanga kulandira katoni ya Nyunzi monga timazitchulira nthawi imeneyo. Zimalembedwa kuti 'Contender' ndipo dzina la Raymond Jackson limapezeka mu izo. Ine sindimatha kuwerenga chingerezi mochuluka. Patsogolo pake mu mauthenga ena a M'bale Branham ndimamumva iye akutchulapo dzina la Junior Jackson, koma sindinathe kulumikiza Junior Jackson ndi Raymond Jackson ngati munthu m'modzi. Bambo wanga sanalankhulepo chirichonse cha munthu ameneyi. Nthawi zina ndimatha kuwerenga pang'ono koma sindimamvapo chirichonse ndipo ndinali wang'ono mu uzimu. Bambo wanga nthawi zonse amalalikira ndi kuchitira umboni ndipo mpingo unakuladi. Palibe mlendo amene amafika ku nyumba kwathu ndi kupita osagawiridwa Mau. Linali gawo la moyo wake – kuchitira umboni. Ndi abale ena ife tinayamba kupita ku malo osungirako anthu othawa nkhondo kukalalikira.

Nditatsiriza sukulu ya Sekondare, Ine ndinakwatira Julie Malunga mu 1996. Mu kachitidwe ka mpingo wa mu m'bado kumene analibe vumbulutso loti Mau ali omwewo chiphunzitso komanso langizo, ine ndinauzidwa kuti ndilape ndipo ndinalapa. Linali lamulo kuti membala aliyense wa mpingo akwatire mu tchalitchi yomweyo. Alongo achichepere ena amaikidwa padera kusungira alaliki achinyamata. Amakhulupirira kuti alaliki adzikwatira anamwali, koma mu zoona zake, atsikana aang'ono amenewo samakhala moyo wa Mau. Julie amachokera ku banja losauka, koma ine ndinamukonda iye. Kenako ine ndinapita kukachita maphunziro a zaka zitatu ophunzitsa ku Sukulu ya Pulaimare. Ine nditatsiriza ndinatumizidwa ku Mwanza, ku Malawi kukagwira ntchito. Kenako ndinakwezedwa kukaphunzitsa ku Sukulu ya Sekondare.

Ine ndinalota mu 1998, za M'bale amene amagwira ntchito ku Queen Elizabeth mu mzinda wa Blantyre, Malawi ndipo anali atatumizidwa ku Japan kukapitiriza maphunziro akundiuza ine kuti ndikuyenera kuima mu Mau. Sindimadziwa chimene chinali ndipo pamene ndinafunsa za M'baleyo anthu anati iye ali ku Japan. Kenako cha kumapeto kwa chaka chimenecho, ine ndinachita ngozi ndipo anthu anai anafa pa malo omwewo. Ine ndinatengedwa kupita ku chipatala cha Queen Elizabeth ndipo M'baleyu anali woyamba kudzandiona ine. Iye anati…, Mulungu akupatsanso mwai wina gwiritsa ntchito bwino mwai umenewu." Mu mtima mwanga ine ndinati ndi mwai wachitatu chifukwa ndinakumbukira nthawi imene ndinali wa zaka ziwiri ndipo ndinapsa ndipo ndinali ndi mabala mpaka makolo anga analibe chiyembekezo. Nditachira ku mabala a ngozi ndinakhala msilikali weniweni wa Ambuye. Ine ndinayamba kumapita ku Mozambique kumakalalikira Mau komanso malo ena. Popeza kuti ndiri wang'ono ndimatha kutsagana ndi ena kukalalikira ku malo osungirako othawa nkhondo, ine ndinatha kudziwa ena amene anabwerera kwao ku Mozambique.

Ine ndinali Dikoni ku mpingo umene M'busa wake anali M'bale Montfort Pemba. Iwo amakhala ndi chisankho cha ma Dikoni ndi maudindo ena chaka chiri chonse. Ndikuyamika Mulungu chifukwa tsopano tikudziwa za Dongosolo la Mpingo ndi zinthu zina. Mu chaka cha 2001, ife tinayamba kagulu kanthu kakang'ono kutsutsana kutabuka mu mpingo umene alaliki samalalikira chinthu chofanana. Mlaliki wina anati M'bale Branham anati ofesi ya mkazi ndi ku Kitcheni ndipo ana a akazi sakuyenera kuphunzira mochuluka kuti asadzapeze ntchito chifukwa akatero zidzawachotsa iwo mu ofesi yawo ku kitcheni monga ananenera Mneneri. Dongosolo la mpingo linali kuti tepi ya M'bale Branham iseweredwe otsogolera nyimbo asanayambe kutsogolera, kenako abwere mlaliki. Iwo amati akukopera izi kuchokera ku Jeffersonville, Indiana. Aliyense anali ndi ufulu wolalikira chirichonse afuna bola ngati atawerenga izo mu mabukhu a Mau Olankhulidwa. (Spoken Word Books) Zimaoneka ngati anthu samadziwa kolowera chifukwa wina sabata ino amatha kuwerenga pamene M'bale Branham anati Television sichinthu chabwino ndipo ndikanatha kuchiombera. Ndipo wina sabata lotsatira ndi kubwera kuwerenga pamene M'bale Branham anati, "Ngati Television ili yoipa, ndiyenso wailesi, nyunzi ndi telefoni ndi zoipa. Zimangosokoneza anthu. Ine ndikuzindikira tsopano kuti simungathe kupitirira opanda utsogoleri. Kuphatikizanso zinthu zina, kagulu kathu, New Testament Assembly, kanayambika.

Mu 2001, Ine ndinaitana M'bale Wilton Mkandawire kudzatilalikira. M'bale winanso Kelvin Matengo anali wolimbikitsa. Ku Africa kuli vuto la malamulo a mpingo kapena kuti konsitishoni. Iwo amene analembetsa mpingo ku Malawi anaulembetsa iwo ngati Bible Believer, ndipo anali nawo ufulu wonse kunena kuti inu simuli gawo la ife. Pofuna kusunga izi ife timayenera kukhala ndi anzathu ngati iwo a ku Lilongwe amene akanatha kutiikira kumbuyo. Ife timakhumba tikanakhala ndi konsitushoni yathu potero pamasoweka ena akhale ngati ma Trustee athu komanso zimatengera kukakomana ndi Loya zimene ngati kagulu kakang'ono sitikanatha. Izi ndi zimene Boma limafuna kuti ligwire ntchito yake bwino koma Mulungu samazifuna. Ichi chinali chida chawo choopsezera chifukwa iwo amatengera zimene zinachitika kuno ku Malawi cha m'ma 90 pamene okhulupirira analowa mu ndende. Ichi ndi chotchinga chachikulu chifukwa kuima kwa pakokha kwa mpingo kukuonongedwa ndi iwo amene akusunga konsitushoni, ndipo iwo amalamulira chimene sichikuyenera kuchitika. Ndi kachitidwe ka Chinikolai.

Kenako mu 2005, pamene M'bale Ben Howard anabwera ku Malawi, ine ndinakhala nawo ku misonkhano ku Blantyre. Kuchokera ku maulaliki ake ine

ndinafulumizika. Ine ndinalandilako mabukhu ake komanso ndinalemba adiresi yanga mu ka bukhu, kenako ndinalandira matepi komanso mabukhu kuchokera kwa M'bale Ben. Mulungu anatsegula maso anga ndipo ndinayamba kulumikiza madontho. Ine ndinayamba kuziona zinthu bwino bwino komanso ndikuona malo a M'bale Jackson. Ine ndimatha kuona chifukwa chiyani iwo a mukachitidwe ka m'bado wa mpingo sakutha kuyenda. Ine ndimatha kuona dongosolo la chiombolo la Mulungu komanso kuona Uthenga mibado ya mipingo itatha. Ine ndinayamba kumasulira mabukhu ndipo izi zinapangitsa kusintha dzina la Mpingo wathu kukhala New Testament Assembly. M'bale Ben sanabweretse zoti tichite ndi zoti tisachite koma iye anangopemphera kuti Mulungu andionetsere njira. Ine ndinapita kunyumba ku banja lathu kukawawonetsera choonadi. Ndi pemphero langa kuti Mulungu tsiku lina adzawatsegula maso ndipo adzathe kukwera sitepe pamwamba. Iwo amadziwa za M'bale Jackson..., komanso Baibulo linapezedwa limene Bambo anga analandira zaka zapitazo ndipo mkati linalembedwa Ben Howard. Bambo anga anati, "Munthu ameneyi amanditumizira Baibulo zaka zapitazo." Ndi chiyembekezo changa kuti Mulungu adzaziulura izo kwa iwo, chifukwa kwa anthu ena zimatenga nthawi yaitali.

Mulungu wandidalitsa ine ndi ana anai, Debora 11, Sharon 7, Esther 4 ndi Andrew Chaka chimodzi ndi miyezi 11. Ine ndiri ndi alongo anga atatu Ethel (Mrs Manda), Emily (Mrs. Damaliphetsa), ndi Mercy (Mrs. Simbeye) ndi m'chimwene m'modzi Caleb. Onsewa ndi okhulupirira a uthenga wa M'bale Branham ndipo onsewa kuphatikiza makolo anga adakali mu kachitidwe ka m'bado wa mpingo ndipo akulalikira kuti M'bale Branham ndi Mneneri wotsiriza wa Mulungu. Ukawafotokozera za utumiki usanu amati amakhulupirira iwo, koma pamene mubweretsa zakuya iwo sangazitenge.

Ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha utumiki umene Iye wandipatsa, ndipo ine ndikulalikira Mau a Mulungu a mu nthawi ino. Ine ndikuthokoza Iye chifukwa cholora maso anga kupenya kuti kuchokera pa Chivumbulutso 10:7 mavesi akupitirira mpaka vesi 8-11, ndipo izo ndi za nyengo ya nthawi imene ife tikukhala, kutitengera ife ku Aefeso chaputala 4:11. Ine tsopano ndi kudziwa kuti 1 Atesalonika 4:16 akukamba za magawo a kubwera Kwake, Mfuwu, Mau a Mngelo Wamkulu ndi Lipenga la Mulungu. Ine tsopano ndikudziwa za Chilungamo cha Mulungu, Chisomo cha Mulungu, Chovala cha Mkwatibwi wa Khristu, Sabata la 70 la Danieli ndi zimene zidzachitike mu gawo loyamba la sabata komanso gawo lotsiriza komanso mavumbulutso ambiri.

Ambuye akudalitseni pamene mukuwerenga umboni wanga.
Wobisidwa mu Uthenga wa Yesu Khristu,
Enoch Kamanula.